# ZOKHUDZA KUSAMALA

Kusamala Institute of Agriculture and Ecology (Kusamala) ndi bungwe la chi Malawi, lomwe si la boma limene limalimbikitsa permaculture ya m'manyumba ndi malimidwe wosamala chilengedwe m'Malawi kudzela mu chiwonetselo, maphunzilo, kufikila madela ena, komanso kulumikizana ndi kufalitsa mauthenga.

Loyamba m'chaka cha 2009, Kusamala imayang'anila chiwonetselo cha permaculture chichikulu kwambiri m'dziko la Malawi, chotchedwa Nature's Gift Permaculture Centre. Kudzela mu chiwonetselo chimenechi Kusamala imaphunzitsa anthu, ndi magulu momwe angapititsile patsogolo madyedwe abwino, kapezedwe ka chuma, ndi kusamala chilengedwe.

Kudzela mu zithandizo ndi ndondomeko zina, Kusamala imafikila madela ena, kuchita kafukufuku ndi kufalitsa mauthenga ndi cholinga chowonetsa kuthekela kwa permaculture ngati njira ya malimidwe ya pa mudzi ndi dziko.

Mdziko limene 80% ya chiwelengelo cha anthu onse ndi alimi ang'onoang'ono, Kusamala imawonetsela momwe zinthu zopezekelatu kumudzi zingafikile kukwanilitsa zofuna za anthu, ndi kupititsa patsogolo umoyo wa anthu ndi chilengedwe.

*Zokolola ku dimba lathu la masamba zolimidwa mwa chilengedwe.*



# LUMIKIZANANI NAFE PA

Mukafuna kudziwa zambiri pa maphunziro athu, madimba athu, kapena kutidziwitsilatu ngati mukufuna kudzawona malo athu motsogozedwa ndi mphunzitsi wa permaculture, chonde lembani uthenga ndi kutumiza ku: info@kusamala.org

Lembetsani ndondomeko yathu ya ma veg box ndi kusangalala ndi ndiwo zamasamba zochokela ku madimba athu amasamba. Lumikizananani nafe pa: garden@kusamala.org


Tipezeni ku msika wa alimi ku Sanctuary Lodge loweluka lotsiliza lililonse la pamwezi, komanso ku Kumbali Cultural Village Flea Market sabata la pakati pa mwezi lililonse.

Kusamala Institute of Agriculture and Ecology

@Kusamala

### MOMWE MUNGATIPEZELE

Kuchokela ku site senta ya Lilongwe, tengani mseu wa Presidential umene ukulunjika ku nyumba ya chifumu ndipo khotani ku manzele pafupi ndi chipata cha nyumba ya chifumuyi. Tsatilani mseuwo pafupifupi ma 5km, Kusamala ikhala ku manja kwanu.




Map by google maps

**Khalani tchelu ndi zomwe zikuchitika ku Kusamala:**

**www.kusamala.org**

# KUSAMALA

INSTITUTE OF AGRICULTURE & ECOLOGY

**Nature's Gift Permaculture Centre**



# Mlozo wa panokha

*Zinkhowe m'mdimba lathu la pakhomo*

# MLOZO WOTSOGOLELA

Tsamba ili ndi lanu kuti musunge. Linakonzedwa kuti likutsogoleleni pa malo athu achiwonetselo cha permaculture ndi kukupatsani mauthenga okhudza ntchito yathu.

Gwiritsani ntchito kalozela uyu pakupeza malo 15 amene ali pano amene akulingana ndi awa awonetsedwa pa kalozelayu.

Pa malo ambiri mupezapo chikwangwani chimene chikupatseni uthega wochuluka wokhudzana ndi chiwonetselo chilichonse.

Chonde musayende pa bedi la mbeu kapena pamene palibe njira.
Chonde tsekani zipata kapena zitseko momwe munazipezela.
Chonde tayani zinyalala mu malo wotaya zinyalala amene apelekedwa.

Tikhulupilira mukhala bwino ndi kusangalala pakuphunzila kwanu.

I — Uthenga ndi poyambila kuyenda

P — Poyimika galimoto

100% RECYCLED
Made from recycled material
FSC www.fsc.org FSC® C006548

1. Dimba la pakhomo
2. Mingóma ya njuchi
3. Dimba la mankhwala
4. Nyumba yo phunziliramo
5. Munda
6. Green house
7. Nazale ya mitengo
8. Manyowa a kompositi
9. Dimba la mbeu zamsika
10. Nkhokwe
11. Dzenje la nthochi
12. Chitetezo mbaula
13. Bwalo la nkhuku
14. Zimbudzi za manyowa
15. Dimba la anthu wokhalila pa malo ano




Mothandizidwa ndi
The Scottish Government
climate futures
The James Hutton Institute

This guide map is based on a GIS mapping exercise undertaken by Julia Reynolds, Austin Dunn and Asa Strong.
Illustration by Sabine Hellmann.